# Thumba la VCF lisintha miyoyo ya alimi ku Chiradzulu

WOLEMBA:
ANDREW MTUPANYAMA

Thumba la Village Challenge Fund (VCF) lomwe unduna wa zamalimidwe ukuyendetsa layamba kubala zipatso m'madera amene inakhazikitsidwa.

Thumba la VCF ndi gawo limodzi lolimbikitsa malimidwe amakono mosaononga chilengedwe la Sustainable Agricultural Production Programme (Sapp).

Alimi a m'mudzi wa Gilinjala kwa mfumu yayikulu Mpama ku Chiradzulu akusimba lokoma ndi ulimi wa soya.

Alimiwa, omwe ali pa gulu la anthu 18, ati anayamba ulimi wawo atamaliza maphunziro ku sukulu yophunzitsa ulimi ngati bizinesi(Farm Business School).

Wapampando wa gululi Fanuel Ntakanya anati gulu lawo linayamba ndi mpamba ochokera ku VCF umene unawathandiza kupeza mbewu ndi zipangizo zina zolimira mahekitala 6.7.

"Nthawi imene tinkayamba, tinalandira K1.4 miliyoni. Titalowetsa ndalama zina mu ulimi wa soya, tinatsala ndi K200 000.00. Tinakolola matumba 90. Matumba 40 anachokera ku munda omwe tinalima pa gulu ndipo 50 anachokera ku minda yomwe membala aliyense analima payekha," analongosola Ntakanya.

Iye anati mamembala ambiri anachita zaphindu ndi ndalama zimene anapeza.

"Ambiri anagula mbuzi ndi nkhumba pomwe ena anagula malata," anatero Ntakanya.

Iye anati ngakhale izi ziri choncho, gulu lawo linakumana ndi mavuto ambiri monga kujomba ku zokambirana zokasamalira munda wagulu komanso kusowa kwa misika.

Msungichuma wa gululi Judith Sapuwa anati waphunzira kuti adzipezeratu misika mbewu zisanache komanso kusayinirana ndi ogula kuti mitengo isasinthe ngakhale patachitika china chake.

"Ku sukulu ya zaulimi tinaphunzira kuti tizipezeratu misika kuopa kuuzidwa kuti tachedwetsa kupititsa mbewu ku msika pamene tikudikira kuti ziume bwino," anatero Sapuwa.

Iye anati chaka chino agwirizana kale ndi makampani ogula mbewu amene ena mwa iwo alonjeza kugula soya osachepera matumba 50.

Ngati zonse zitayenda bwino, matumba 50 amenewa akhoza kubweretsa ndalama zokwanira K2.5 miliyoni.

Gululi lati liri ndi masomphenya oyamba kupanga zakudya za ziweto kuchokera ku soya.

Thumba la VCF ndi njira yolimbikitsira alimi omwe ali magulu kuti apeze ndalama zomwe zingawatukule kufika pa mlingo odalira ulimi ngati bizinesi kudzera mu ulimi wamakono komanso kukonza katundu osiyanasiyana kuchokera ku zokolola.

Kudzera mu ndondomekoyi, unduna wa zamalimidwe ukufunanso kuchulukitsa zokolola za alimi, phindu komanso kulimbikitsa thanzi labwino m'maanja a alimi aang'onoang'ono.

Malingana ndi mlangizi wa zaulimi mu chigawo cha ulimi cha Mbulumbuzi Extension Planning Area (EPA) Margaret Nkuziona, boma linapereka ndalama ku magulu osiyanasiyana m'bomalo kuti atukulire magawo osiyanasiyana.

Iwo anati magulu ena anasankha kulima soya pomwe ena anasankha ulimi wa ziweto monga mbuzi ndi nkhuku.

Dongosolo la SAPP likugwira ntchito za VCF mu maboma a Blantyre, Balaka, Chiradzulu, Chitipa, Lilongwe ndi Nkhotakota. ■



CHITHUNZI: ANDREW MTUPANYAMA

Mmodzi mwa alimi omwe akupindula

## KODI MUKUDZIWA?

Kodi mukudziwa kuti kusungira nthochi zakale kukuchititsa kuti chisaka cha nthochi chizitsetsabe nthochi m'dziko muno? Nanga mukudziwa kuti nthochi zopanda matenda zomwe a unduna wa zaulimi akulimbikitsa m;dziko muno ndizokoma kngati zakale zija? Tiyeni tidzule nthochi zakale tibzale zopanda matenda kuti tipindule ■

KALIMALIMA James Kazembe

